

CHISOMO, CHIKONDI NDI CHIYANJANO



Phunziro 13, September 26, 2026




“Chisomo cha
Ambuye Yesu
Khristu, ndi
chikondi cha
Mulungu, ndi
chiyanjano cha
Mzimu Woyera
zikhale ndi inu
nonse.”

(2 Akorinto 13:14, CCL)

Mawu amene Paulo anakonda kugwitsa ntchito kwambiri kumapeto amakalata ake, ndipo anawagwitsa ntchito mosiyana pang'ono m'makalata 13 mwa makalata ake 14, ndi awa: “Chisomo cha Ambuye wathu Yesu Khristu chikhale nanu” (Aroma 16:24; 1 Akorinto 16:23; Agalatiya 6:18; Aefeso 6:24; Afilipi 4:23; Akolose 4:18; 1 Atesalonika 5:28; 2 Atesalonika 3:18; 1 Timoteyo 6:21; 2 Timoteyo 4:22; Tito 3:15; Filemoni 1:25; Ahebri 13:25).

Komabe, mu kalata yachiwiri yopita kwa Akorinto, Paulo anamaliza mwanjira yapadera kwambiri. Mawu ake otsanzikana akuphatikizapo chisomo, chikondi, ndi chiyanjano cha onse atatu a Umulungu: Mwana, Atate, ndi Mzimu Woyera (2 Akorinto 13:14).



“Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu”



“Chikondi cha Mulungu”



“Chiyanjano cha mzimu Woyera”



“Zikhale ndi inu nonse”

“CHISOMO CHA AMBUYE YESU KHRISTU”

“Pakuti mudziwa chisomo cha Ambuye wathu Yesu Khristu, kuti, chifukwa cha inu anakhala wosauka, angakhale anali wolemara, kuti inu ndi kusauka kwake mukakhale olemara.” (2 Akorinto 8:9)

Paulo akuyamba ndi kumaliza Kalata yake Yachiwiri kwa Akorinto potchula chisomo cha Yesu (2 Akorinto 1:2; 13:14). Kodi chisomo chimenechi chimatanthauza chiyani?



Iye anasiya chuma chosatha cha Kumwamba ndipo anakhala wosauka kuti ife tilandire chuma chake monga cholowa (2 Akorinto 8:9).



Iye anayenda m'dziko lathu kuti ife timudziwe, timukonde, ndi kutsatira chitsanzo chake (Yohane 15:12)



Iye anadzichepetsa ndipo anakhala womvera mpaka imfa, kuti atikhululukire machimo athu ndi kutipatsa moyo wosatha (Afilipi 2:8)

Kodi n'chiyani chimachitika kwa ife amene timalandira chisomo chake?

Timayesedwa olungama (Aroma 3:24; Aefeso 1:7)

Timakondwera m'chiyembekezo (Aroma 5:2)

Timalandira mphamvu kuchokera kwa Khristu (2 Akorinto 12:9)

Utchimo ulibe ulamuliro pa ife (Aroma 6:14)


Tidzalamulira pamodzi ndi Yesu m'moyo (Aroma 5:17, 21)



“CHIKONDI CHA MULUNGU” (1)

“Iye wosakonda sazindikira Mulungu; chifukwa Mulungu ndiye chikondi.” (1 Yohane 4:8)

Baibulo limanena momveka bwino kuti Mulungu ndiye chikondi (1 Yohane 4:8). ye waonetsa chikondi chimenechi pa zolengedwa zake zonse. Tikhoza kuchiwona m’mitima mwathu; mu ubale wa pakati pa makolo ndi ana; m’maluwa okongola; komanso m’mbalame zoimba mokoma; ...



Paulo anaphunzitsa Akorinto (komanso ife) kuti chikondi chimamanga (1 Akorinto 8:1); kuti popanda chikondi palibe chilichonse chimene chili ndi phindu (1 Akorinto 13:1-3); komanso kuti zonse zimene timachita ziyenera kuchitidwa ndi chikondi chimene chimachokera kwa Mulungu (1 Akorinto 16:14).

Koma, mosakayikira, kusonyeza kwakukulu kwa chikondi cha Mulungu kungawonekere mu kupereka kwa Yesu ngati nsembe ya machimo athu (Yohane 3:16).

Chitsanzochi chimatichititsa kuchitira ena zinthu mwachikondi chomwecho chimene Mulungu watisonyeza (1 Yohane 3:16).

“CHIKONDI CHA MULUNGU(2)

“Chotsalira, abale, kondwerani. Muchitidwe angwiro; mutonthozedwe; khalani a mtima umodzi, khalani mumtendere; ndipo Mulungu wa chikondi ndi mtendere akhale pamodzi ndi inu.” (2 Akorinto 13:11)

Paulo akuonetsa Mulungu m'njira zosiyanasiyana:



“Mulungu Wopirira” (Aroma. 15:5)



“Mulungu wa chiyembekezo” (Aroma 15:13)



“mulungu wa mtendere” (Aroma. 15:33)



““Mulungu [...] wa chifundo” (2 Akorinto 1:3a)



“Mulungu wa chitonthozo chonse” (2 Akorinto 1:3b)



“Mulungu wa chikondi” (2 Akorinto. 13:11)



Mulungu sikuti ali ndi makhalidwe amenewa chabe, koma lye ndiye gwelo limene makhalidwe onsewo amachokera kufika kwa ife.

Monga momwe taonera, Mulungu ndiye chikondi, komanso lye ndi Mulungu wa chikondi; kutanthauza kuti:



Mulungu Atate
amatipatsa
chikondi chake
(1 Yohane 3:1)



Mulungu Khristu
amatidzaza ndi chidzalo
cha chikondi chake
(Aefeso 3:19)



Mulungu Mzimu Woyera amatsanulira
chikondi chake pa ife (Aroma 5:5)

“CHIYANJANO CHA MZIMU WOYERA”

“Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu, ndi chikondi cha Mulungu, ndi chiyanjano cha Mzimu Woyera zikhale ndi inu nonse.” (2 Akorinto 13:14)

Paulo akufuna kuti zinthu izi zikhale ndi ife: chisomo cha Munthu (Ambuye Yesu Khristu); chikondi cha Munthu (Mulungu); ndi chiyanjano... cha mphamvu kapena cha Munthu? (2 Akorinto 13:14). Kutu mawuwa agwirizane bwino, Paulo akulankhula za Munthu (Mzimu Woyera), osati mphamvu.

M'mawu ake oposa 40 onena za Mzimu Woyera m'makalata ake kwa Akorinto, Paulo akufotokoza Mzimu Woyera kuti ali ndi makhalidwe a munthu, osati ngati mphamvu chabe yochokera kwa Mulungu:



Amakonzekeretsera anthu kuti agwire ntchito ya utumiki (1 Akorinto 2:4)

Amatiulirira zinthu zakuya za Mulungu (1 Akorinto 2:10)

Amatiphunzitsa (1 Akorinto 2:13)

Amakhala mwa ife (1 Akorinto 3:16)

Amagwira ntchito limodzi ndi Khristu kuti tiyesedwe olungama (1 Akorinto 6:11)

Amapereka mphatso zauzimu (1 Akorinto 12:7-11)

Amatisindikiza chizindikiro cha chipulumutsotsidwe (Akorinto 1:22)

Amalemba malamulo m'mitima mwathu (2 Akorinto 3:3)

Amatipatsa moyo watsopano mwa Khristu (2 Akorinto 3:6)

Amatimasula ku uchimo (2 Akorinto 3:17)


“ZIKHALE NDI INU NONSE”

“monga mwa kudziwiratu kwa Mulungu Atate, m'chiyeretso cha Mzimu, chochitira chimvero, ndi kuwaza kwa mwazi wa Yesu Khristu: Chisomo, ndi mtendere zichulukire inu.” (1 Petro 1:2 NIV)

Ngakhale kuti tazolowera kutchula Utatu (Anthu atatu a Umulungu, Mulungu mmodzi) motsatira dongosolo lakuti “Atate, Mwana, Mzimu” (Mateyu 28:19), Paulo akuwatchula kuti “Mwana, Atate, Mzimu” (2 Akorinto 13:14), ndipo Petro akuwatchula kuti “Atate, Mzimu, Mwana” (1 Petro 1:2).



Palibe dongosolo la maudindo apamwamba ndi apansi pakati pawo; aliyense amangogwira ntchito yosiyana mu ndondomeko ya chipulumutso, koma onse ali ndi makhalidwe ndi zolinga zofanana.



Choncho, Paulo akumaliza kalata yake pofuna kuti chisomo, chikondi, ndi chiyanjano cha Umulungu wonse zikhale ndi ife tonse(2 Akorinto 13:14).

“Atate sangathe kufotokozedwa ndi zinthu za padziko lapansi. Atate ali ndi chidzalo chonse cha Umulungu, ndipo saoneka ndi maso a anthu amene amafa. Mwana ali ndi chidzalo chonse cha Umulungu choonetsedwa[...] Mtonthozi amene Khristu analonjeza kutumiza atakwera Kumwamba, ndiye Mzimu wokhala ndi chidzalo chonse cha Umulungu, amene amaonetsa mphamvu ya chisomo cha Mulungu kwa onse amene amalandira ndi kukhulupirira Khristu monga Mpulumutsi wawo waumwini.

Pali anthu atatu amoyo mu Utatu wakumwamba; mu dzina la mphamvu la zazikulu zitazi—Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera—anthu amene amalandira Khristu mwa chikhulupiriro chenicheni amabatizidwa, Ndipo mphamvu zimenezi zidzagwira ntchito limodzi ndi anthu omvera a Kumwamba pamene akuyesetsa kukhala ndi moyo watsopano mwa Khristu.”